PHUNZIRO LA 24

1. Mkazi wa Abulahamu, Sara, atamwalira, kodi Abulahamu anachita chiyani pomutonthoza mwana wake Isaki?
-Abulahamu anamutonthoza pomupatsa iye mkazi.

2. Kodi dzina la mkazi wa Isaki linali ndani?
-Rabeka.

3. Kodi mayina a ana aŵiri a mapasa amene Rabeka anabereka anali ndani?
-Esau ndi Yakobo.

4. Kodi Mulungu anazidziŵa bwanji zonse za Esau ndi Yakobo asanabadwe?
-Mulungu amazidziŵa zonse za anthu onse.
-Palibe chobisika kwa Mulungu.

5. Kodi Esau amkakhulupilira mwa Mulungu?
-Iyayi.

6. Kodi Yakobo amkakhulupilira mwa Mulungu?
-Inde.

7. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anasankha zotumiza Mpulumutsi kupitira mwa zidzukulu za yakobo?
-Chifukwa chakuti Esau samkakhulupilira mwa Mulungu

8. Kodi Yakobo anawona chiyani m'maloto amene Mulungu anamupatsa iye?
-Yakobo anaŵawona makwelero amene pasi pamkakhuza pa dziko la pansi ndipo kumwamba kwa makwelerowo kumkakhuza kamwamba.

-Angelo amkatsika ndi kumakwera pa makweleropo ndipo

Mulungu anali pamwamba pa makwelerowo.

9. M'malotomo, kodi Mulungu amkamuphunzitsa chiyani Yakobo za Mpulumutsi?
-Ngati m'mene Makwelero amkalilumikizira dziko la pansi ndi kumwamba pamodzi, Mulungu adzatumiza Mpulumutsi amene adzaŵabweretse anthu a pa dziko la pansi ndi Mulungu wa kumwamba pamodzi.

10. Kodi chifukwa chiyani Mulungu sangaliyiwale lonjezo Lake lotumiza Mpulumutsi?
-Chifukwa chakuti Mulungu sangayiwale.
-Chifukwa chakuti Mulungu sangasinthe.
-Chifukwa chakuti nthaŵI zonse Mulungu amasunga Malonjezo Ake.

11-Yakobo akukhalabe ku Harani, kodi anabereka ana angati?
-Anabereka ana amuna 12.

12. Yakobo akukhalabe ku Harani, kodi Mulungu anamuwuza iye kuti achite chiyani?
-Mulungu anamuwuza Yakobo kuti achoke ku Harani ndipo abwere ku dziko la kwawo.ku Kanani.

13. Kodi dzina latsopano limene Mulungu anamupatsa Yakobo linali ndani?.
-Dzina latsopano la Yakobo linali Isilayeli.

-Kodi amene amkamutchinjiriza Yakobo mpaka kumubweretsanso kwawo ku Kanani kuchokera ku Harani anali ndani?
-Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 37:1



-Ngakhale kuti mkazi wake wa Potifala anamunamizira Yosefe, Yosefe ankakhulupilirabe mwa Mulungu.

-Ngakhale kuti Yosefe anamuyika mnyumba ya akayidi, Yosefe ankakhulupilirabe mwa Mulungu.

-Kodi amene ankamuyang'anira Yosefe mnyumba ya ukayidi anali ndani?
-Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu amkamuyang'anira Yosefe?
-Chifukwa chakuti Yosefe amkadziŵa kuti anamuchimwira Mulungu.
-Chifukwa chakuti Yosefe amkadziŵa kuti tchimo lake limubweretsera imfa yosatha.
-Chifukwa chakuti Yosefe amkadziŵa kuti Mulungu yekha ndi amene angamupulumutse iye.

-Chifukwa chakuti Yosefe amkakhulupilira kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi kudzamupulumutsa iye.

-Kodi mukuganiza kuti Mulungu adzamuyiwala Yosefe mnyumba ya ukayidi ija?
-Iyayi.

-Mu phunziro lotsatirali, tidzaŵerenga zimene Mulungu anamuchitira Yosefe.

mu ndende m'mene amkasungiramo akayidi a mfumu.

-Potifala atabwelera ku nyumba kwake, anakhulupilira bodza la mkazi wake, ndipo anamuyika Yosefe mnyumba ya ukayidi.

-Yosefe ali mnyumba ya ukayidi, kodi Mulungu anamutaya iye?
-Iyayi.

-Mulungu sadzamutaya munthu aliyense amene akukhulupilira mwa Iye.
-Nthaŵl zonse Mulungu anali ndi Yosefe.

-Ngakhale pamene Yosefe anali mnyumba ya ukayidi, Mulungu anali ndi iye.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 39:20b-23

20-Koma Yosefe ali mnyumba yosungira akayidimo,
21-AMBUYE anali naye; namukomera mtima kwambiri, Kotero kuti osunga ndende anakondwera naye Yosefe.
22-Anamusandutsa kapitawo oyang'anira akayidi anzake onse, pamodzi ndi zonse zochitika mu ndendemo.
23-Zonse zinali m'manja mwa Yosefe, ndipo osunga ndendeyo sankayang'aniranso kanthu kena kalikonse, chifukwa chakuti AMBUYE anali naye Yosefe ndipo amkamukhonzetsa pa zonse zimene ankachita.

-Ngakhale kuti abale ake aYosefe ankamuda Yosefeyo, Yosefe ankakhulupilirabe mwa Mulungu.

-Ngakhale kuti abale ake a Yosefe anamugulitsa Yosefe ngati kapolo, Yosefe ankakhulupilirabe mwa Mulungu.



1-Yakobo anakhalabe ku dziko la kenani kumene bambo ake amkakhala.

-Kodi Yakobo anali ndi ana angati?
-12.

-Yakobo anali ndi ana 12 koma amkamukonda kwambiri mwana m'modzi kuposa ena onse.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 37:3

3-Tsopano Isilayeli amkamukonda kwambiri Yosefe kupambana ana ake ena onse, popeza anali mwana wake wa pa ukalamba. Adamusokera mkanjo wautali wa manja atali.

-Kodi dzina latsopano limene Mulungu anapereka kwa Yakobo linali ndani?
-Isilayeli.

-Kodi dzina la mwana wa Yakobo amene amkamukonda kwambiri kuposa ana ake ena onse linali ndani?
-Yosefe.

-Chifukwa chakuti Yakobo amkamukonda kwambiri Yosefe, iye anamusokera Yosefe mkanjo wawutali wa manja atali.

-Chifukwa chakuti Yakobo amkamukonda kwambiri Yosefe kuposa abale ake ena onse, abale ake a Yosefeyo amkamuchitira msanje.

-Chifukwa chakuti Yakobo amkamukonda kwambiri Yosefe, abale ake a Yosefe amkamuda kwambiri iye.

-Abale ake a Yosefe amkamudanso iye chifukwa chakuti

amkaŵawuza bambo ake zonse zoyipa zimene amkazichita abale akewo.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 37:2 ndi 4

2-Pamene Yosefe anali mnyamata wa zaka 17, ankaweta nkhosa ndi mbuzi pamodzi ndi abale ake, ana a Biliha ndi a Zilipa, akazi awo a bambo awo. Tsopano Yosefe amkaŵawuza bambo ake zoyipa zimene amkachita abale akewo.

4-Abale ake atawona kuti bambo awo amkamukonda [Yosefe] kwambiri kupambana iwowo, adayamba kudana naye Yosefeyo, ndipo samkalankhulana naye mokondwa.

-Kodi chifukwa chiyani anthu ena amaŵakwiyira anthu ena?

-Kodi chifukwa chiyani anthu ena amaŵada anzawo?

-Chifukwa chakuti aliyense anabadwa ali osiyana ndi Mulungu.

-Chifukwa chakuti aliyense anabadwa ndi tchimo mu mtima mwake.

-Chifukwa chakuti aliyense anabadwa ngati mwana wa Satana.

-Abale ake aYosefe amkadana ndi Yosefe chifukwa chakuti anabadwa ali osiyana ndi Mulungu.

-Abale ake a Yosefe amkadana ndi Yosefe chifukwa chakuti aliyense anabadwa ndi tchimo mu mtima mwake.

-Abale ake a Yosefe amkadana ndi Yosefe chifukwa chakuti aliyense anabadwa ngati mwana wa Satana.

-Munthu aliyense anabadwa ali osiyana ndi Mulungu ndipo sitingathe kuzisintha tokha.

-Munthu aliyense anabadwa ali ndi tchimo mu mtima



bwalo, kusiya muyinjiro uja uli m'manja mwa mkaziyo.

13-Tsopano mkazi uja atawona kuti Yosefe wasiya muyinjiro wake ndikuthaŵira pa bwalo,

14-adaŵayitana antchito mnyumbamo, naŵawuza kuti, “Mwaziwona izi? Mwamuna wanga anabwera ndi mu Heberi uyu mnyumba muno kudzatipunza ife. Iye anakaloŵa kuchipinda changa nandinyenga kuti ndigone naye. Koma ine ndinakuwa kwambiri.

15-Tsopano atamva kukuwa kwangako, wasiya muyinjiro wake m'manja mwangamu ndikuthaŵira pa bwalo.”

16-Muyinjirowo anangowusunga m'manja mwake kudikira mpaka bwana wa Yosefe atabwera.

17-Tsopano atabwera anamusimbira nkhani yonseyo, anati, “Kapolo uja wa Chiheberi munabwera naye mnyumba munoyu, analoŵa kuchipinda kwanga kukandipunza ine.

18-Koma ine nditakuwa, iyeyo anasiya muyinjiro wake pafupi ndi ine, mkuthaŵira pa bwalo.”

-Chifukwa chakuti Yosefe ankakhulupilira mwa Mulungu, iye anakana kugona ndi mkazi wa Potifala.

-Chifukwa chakuti Yosefe anakana kugona ndi mkazi wake wa Potifala, mkazi wake wa Potifala anamunamizira Yosefe.

-Kodi chinachitika chiyani Potifala atabwelera ku nyumba kwake?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 39:19-20a

19-Mbuye wake wa Yosefe anapsa mtima koopsa atamva mawu a mkazi wake onena kuti, “Inde, izi ndi zimene wandichita kapolo wanu.”

20-Pompo anamumangitsa Yosefe nakamutsekera

kalikonse, koma chakudya chokha chimene ankadya.

-Ngakhale kuti abale ake a Yosefe anamuda Yosefe kwambiri, Mulungu sanamutaye Yosefe.

-Ngakhale kuti abale ake a Yosefe anamugulitsa Yosefe ngati kapolo, Mulungu sanamutaye Yosefe.
-Chifukwa chakuti Yosefe ankakhulupilira mwa Mulungu, Mulungu anamudalitsa Yosefe.

-Tsiku lina, Potifala atachoka, china chake chinachitika kwa Yosefe.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 39:6b-18

6-Yosefe anabadwa ndi thupi labwino ndipo anali okongola,
7-Ndipo patapita kanthaŵl, mkazi wa bwana wake anayamba kumusilira Yosefe. Tsopano mkaziyo ana-muwuza Yosefe kuti, “ Bwanji ugone ndi ine?”
8-Koma Yosefe anakana, ndipo anati, “Chifukwa chakuti ine ndikugwira ntchito muno, bwana wanga sala-badiranso kanthu kalikonse mnyumba muno. Adandipatsa ukapitawo oyang’anira zake zonse.
9-Ndipo ulamuliro onse wa mnyumba muno uli m’manja mwanga, osati m’manja mwake. Sanandimane kanthu kena kalikonse kupatula inu nokha, pakuti ndinu mkazi wake. Tsopano kungatheke bwanji kuti ine ndichite chinthu chiyipitsitsa choterechi ndi kuchimwira Mulungu?”
10-Ngakhale kuti mkazi uja amkalankhula mawu amenewa kwa Yosefe tsiku ndi tsiku, Yosefeyo samkalola mpang’ono pomwe kuchita naye zoyipazo.
11-Koma tsiku lina Yosefe analoŵa mnyumba kuti agwire ntchito, ndipo panalibe antchito ena mnyumbamo.
12-Mkazi uja anagwira muyinjiro wa Yosefeyo, na-muwuza kuti, “Ugone nane basi!” Koma iye anathaŵira pa



mwake ndipo sitingathe kuzisintha tokha.

-Munthu aliyense anabadwa ali mwana wa Satana ndipo sitingathe kuzisintha tokha.

-Tsiku lina, Mulungu anamupatsa Yosefe maloto.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 37:5-8

5-Tsiku lina Yosefe analota maloto, anaŵafotokoze-ra abale ake malotowo. Zitatero abale akewo anadana naye kupambana kale
6-Iye adaŵawuza kuti, “Mverani maloto amene ndalota:
7-Tonsefe tinali m’munda, ndipo tinali kumanga mi-tolo ya tirigu. Tikumamanga chomwecho, mtolo wanga unayimilira. Ndipo mitolo yanu inawuzungulira mtolo wangawo ndikumawuŵeramira.”
8-Apo abale akewo anamufunsa kuti, ”Kodi ukugani-za kuti udzakhala mfumu yathu? Kodi ndiye kuti iweyo mkudzatilamulira ifeyo?” Chomcho anadana naye kwambi-ri kuposa kale chifukwa chifukwa cha malotowo ndi mau akewo.

-Kodi maloto amene anapereka Mulungu kwa Yosefe anali otani?

-M’malotowo, Yosefe ndi abale ake amkamanga mitilo ya tiligu ku munda.

-Kenako, mitolo ya tiligu ya abale ake a Yosefe, anaŵeramira mtolo wa tiligu wa Yosefe.

-Chifukwa cha maloto amene Mulungu anamupatsa Yosefe, abale ake a Yosefe anapambana kumuda iye kwambiri.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 37:9-11

9-Chomcho Yosefe analotanso maloto ena, ndipo anaŵawuzanso abale akewo kuti, “Ndalotanso, ndipo ndawona dzuŵa, mwezi ndi nyenyezi khumi ndi imodzi zikundiŵeramira.”

10-Maloto amenewa anaŵawuzanso bambo ake pamodzi ndi abale ake omwe aja. Atate akewo anamudzudzula, anati, “Kodi maloto ameneŵa ndi otani? Kodi ukuganiza kuti ine, mayi ako pamodzi ndi abale akoŵa, tidzakugwadira iwe?”

11-Tsopano abale ake aja anachita naye msanje kwambiri. Koma atate ake amkakhala akuganizirabe za zimenezi.

-Kodi maloto achiŵiri amene Mulungu anapereka kwa Yosefe anali otani?

-M’malotowo, munali dzuŵa, mwezi, ndi nyenyezi khumi ndi imodzi.

-Kenako, dzuŵa, mwezi ndi nyenyezi khumi ndi imodzizo zinamuŵeramira Josefe.
-M’malotowo, kodi amene anali dzuŵa ndani?
-Bambo ake a Yosefe.

-M’malotowo, kodi amene anali mwezi ndani?
-Mayi ake aYosefe.

-M’malotowo, kodi amene anali nyenyezi khumi ndi imodzi ndani?
-Abale ake a Yosefe amene anali khumi ndi m’modzi.

-Kodi maloto onsewo amkatanthawuza chiyani?

-Tsiku lina, Mulungu adzamupatsa ufumu Yosefe, ndipo



Tiyeni tiŵerenge Genesesi 39:1

1-Tsopano a Isimayele aja anapita naye Yosefe ku Ejipito kumene Potifala mu Ejipito, nduna yayikulu ya Falawo ndiponso mkulu wa asilikali olondera ku nyumba ya mfumu, adamgula.

-Kodi anthu a malonda a ukapolo aja anamugulitsa Yosefe kwa ndani?
-Kwa Potifala.

-Kodi Mulungu anamusiya Yosefe?
-Iyayi.
-Mulungu sadzamusiya munthu aliyense amene akukhulupilira mwa Iye.

-NthaŵI zonse Mulungu anali ndi Yosefe.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 39:2-6a

2-AMBUYEanali naye Yosefe, ndipo anamuthandiza kuti zonse zimuyendere bwino. Ndipo ankakhala mnyumba ya bwana wake, mu Ejipito uja.

3-Bwana wakeyo atawona kuti AMBUYE anali naye Yosefe, ndipo kuti ankamukhozetsa pa zonse zimene ankachita,

4-Potifala adakondwa naye Yosefe poona m’mene ankamutumikilira. Chomcho adamusandutsa kapitawo wa nyumba yake, ndiponso woyang’anira zonse za m’nyumbamo.

5- Kuyambira nthaŵI imene Yosefe adayamba kusamalira zonse za m’nyumba ya Potifalayo, AMBUYE anadalitsa zonse za ku nyumba kwa mu Ejipitoyo, ngakhalenso za ku minda kwake chifukwa cha Yosefeyo.

6-Chomcho Potifalayo anayika m’manja mwa Yosefe zake zonse; kotero kuti sankalabadiranso kanthu

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 37:32-35

32-Adatenga mkanjowo napita nawo kwa bambo awo, ndipo anati, “Tayang’anani, kapena mkukhala mkanjo wa mwana wani uja.”
33-Yakobo anawuzindikira mkanjowo, nati, “Ha, ndi wakedi! Chilombo chamupha mwana wanga. Kalanga ine, Yosefe wakadzulidwa!”
34-Yakobo anang’amba zovala zake, navala chiguduli mchiwuno, chifukwa cha chisoni. Adalira maliro a mwana wakeyo nthaŵl yayitali.
35-Ana ake onse aamuna ndi aakazi, anabwera kuti amutonthoze koma iye anakana, adati, “Ndidzakhala ndikulira maliro a mwana wanga mpaka ndidzapite kumanda komwe kuli iyeko.” Chomcho adapitilizabe kulira chifukwa cha Yosefe mwana wake.

-Abale ake a Yosefe anamugulitsa iye ngati kapolo.
-Kenako abale ake a Yosefewo anaŵanamiza bambo awo.
-Yakobo ankaganiza kuti Yosefe anamwalira.

-Abale ake a Yosefe ankamuda kwambiriYosefe.
-Chidani chimenecho chinaŵapangitsa abale ake a Yosefe kuti amugulitse iye ngati kapolo.

-Chidani cha abale ake a Yosefe kwa Yosefe, chinaŵapangitsa iwo kuti aŵanamize bambo awo.
-Nthaŵl zonse chidani chimabweretsa machimo ambiri.

-Kodi Yosefe anamwalira?
-Iyayi.

-Kodi Yosefe anali kuti?
Yosefe anali ku Ejipito.



onse a m’banja lake adzamugwadira iye.

-Kodi amene amkadziŵa za tsogolo la Yosefe ndikumuwonetsa Yosefeyo tsogolo lakelo kupitira m’maloto anali ndani?
-Mulungu.

-Ngati m’mene amkadziŵira Mulungu za tsogolo la Yosefe, Mulungu amadziŵanso za tsogolo lathu.

-Kodi Mulungu amadziŵa zinthu zingati za tsogolo lathu?
-Mulungu amadziŵa zonse za tsogolo lathu.

-Chifukwa cha maloto amene Mulungu anamupatsa Yosefe, abale ake a Yosefe anapitilira kumuda kwambiri.

-Tsiku lina, Yosefe anapita kumene abale ake amkadyetsera ziweto zawo.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 37:17b-20

17-Chomcho Yosefe anaŵalondola abale akewo ndipo anakaŵapeza ku Dotani.
18-Abale ake aja anamuwonera kutali, iye asanayandikire mkomwe pamene panali iwopo. Iwo anayamba kumupangira chiwembu natsimikiza kuti amuphe.
19-Onsewo amkawuzana kuti, “Uyotu, kamaloto uja, akudza apoyo!
20-Tiyeni timuphe ndipo mtembo wakewo tiwuponye mchitsime china mwa zitsime zili apazi. Tizikanena kuti wajiwa ndi chilombo, ndipo tidzawona tanthawuzo lake la maloto ake aja.”

-Abale ake a Yosefe anadana naye kwambiri ndipo amkafuna kuti amuphe.

-Koma m'bale wake wa Yosefe woyamba kubadwa, Rubeni, anayesa kumupulumutsa Yosefeyo.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 37:21-24

21-Rubeni atamva zimenezi, anayesa kumupulumutsa iye kuchokera m'manja mwawo. Ndipo anati, "Tiyeni tisamuphe."
22Tiyeni tisamukhetse mwazi wina uli wonse koma tingomuponyera mu chitsime chopanda madzichi mchipululu muno, koma tisamupweteke kose."
Rubeni amkalankhula zimenezi akuganiza kumupulumutsa iye m'manja mwawo, kuti amutumize kwa bambo ake.
23-Chomcho Yosefe atafika kumene kunali abale ake aja, iwowo anamuvula, mkanjo wake, wawutali manja umene anawuvala-
24-namutenga, nkumuponya mchitsime chopanda madzi.

-Kodi abale ake a Yosefe anachita naye chiyani Yosefe?
-Anamuvula mkanjo wake, namuponya mu chitsime chopanda madzi.

-Kodi m'bale wake wa Yosefe, Rubeni, atachoka, abale ake otsalawo anachita chiyani kwa Yosefe?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 37:25-28

25-Pamene iwo amkadya, anawona gulu la a Isimayele akuchokera ku Giliyadi. Ngamira zawo zinali zitasenza mafuta apangira mankhwala ndi zonunkhila zimene amkapita nazo ku Ejipito.
26-Kenako Yuda anaŵafunsa abale ake kuti, "Kodi tipindura chiyani tikamupha m'bale wathuyu ndikubisa, osawulula kuti tamupha?



27-Tiyeni tumugulitse kwa a Isimayeleŵa. Nanga iyeyu sim'bale wathu, thupi limodzi ndiponso magazi amodzi?" Abale akewo adavomereza zimenezo.
28-Kenako a Midiyani ena a malonda anafika pomwepo. Abale akewo anamutulutsa Yosefe uja mchitsime muja, namugulitsa kwa a Isimayelewo pa mtengo wa miyala ya siliva makumi aŵiri, ndipo iwowo anapita naye ku Ejipito.

-Abale ake a Yosefe anamugulitsa iye ngati kapolo kwa anthu a malonda a ukapolo.

-Kodi anthu a malonda a ukapolowo anamutengera kuti Yosefe?
-Ku Ejipito.

-Kodi abale akewo anachita chiyani Rubeni atabwerera?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 37:29-31

29-Rubeni atabwerera ku chitsime kuja, anapeza muli gwaa! Chomcho anang'amba zovala zake chifukwa cha chisoni.
30-Ndipo anabwerera kwa abale ake aja naŵawuza kuti,"Mnyamata ujatu palibe! Tsopani ine ndichite chiyani?"
31-Pomwepo iwo anapha mbuzi naviika mkanjo wa Yosefe uja m'magazi ake.

-Abale ake a Yosefe anatenga mkanjo wa Yosefe, ndipo anapha mbuzi, ndikuwuviika mkanjo wa Yosefeyo m'magazi a mbuziyo.

-Kenako abale ake a Yosefewo anawutengera mkanjo woviikidwa m'magazi a mbuzi uja kwa bambo awo, Yakobo.